

LIU LA NAMIKANGO

Namikango Mission

Volume 20(1), June 2020



Kodi Maso Athu Tipenyetsetse kwa Yani?

Pamene tikuyandikira pakati pa chaka cha 2020, tikhoza kuima kaye ndikulingalira m'mene chakachi chayendera kufikira pano. Chaka chino chakhala chosiyana ndi zaka zina. Pamene chinayamba ndi zokolola zabwino kwa anthu ambiri kuno ku Malawi, mliri wa dziko lonse wasinthiratu m'mene timachitira chilichonse, kuyambira ku kupembedza kutchalitchi ndi kuyendera anzathu ndi abale. Panopa tikukhala m'dziko losiyaniananatu ndi m'mene tinalili kumayambiriro kwa chakachi.

Pamene zinthu zambiri zosintha miyoyo yathu zachitika, ndizosavuta kulunjika maso athu pa zinthu zimenezo ndi kuika chidwi chatu pa zimene zikuchitika kwa ife komanso mozungulira ifeyo. Ndizosavuta kukodwa mu nkhani ndi mu miseche ndi manong'onong'o okhudza nkhani. Kuno ku Malawi, mliriyu ukuchitika pamene dzikoli likulimbananso ndi nkhani za ndale. Zochitika zazikuluzikulu zimenezi zikhoza kudzada m'maganizo mwathu, nzokambirana zathu ndi kutipanga ife kukhala ndi mantha m'mene zinthu zonsezi zithere. Ngati titazilola zimenezi, maganizo a mliri ndi a ndale akhoza kumiza mitu yathu m'maganizo a mantha ndi mkwiyo, pamene tisakumvetsetsa m'mene zimenezi zingathere.

Baibulo lili ndi zambiri zonena zokhudza izi. Chipangano Chakale ndi nkhani imodzi yaikulu ya anthu a Mulungu m'masautso. Anayamba ngati akapolo kumayambiriro, ndipo kumapeto kwa Chipangano Chakale iwo anali

alibe dziko lawolawo, asakudziwika kuti ndi ayani, komanso ufulu wawo. Pamene Israyeli anagonjetsedwa ndi kutengedwa kupita ku ukapolo, iwo analibe chonena chilichonse ngati dziko komanso umoyo wawo unali wosatetezeka. Anthu a Mulungu amadziwa bwino kudutsa m'mavuto andale komanso a zaumoyo!

Komabe mu zinthu ndi mu zochitika zonsezi, amuna ndi akazi a Mulungu anasungabe chikhulupiliro chawo mwamphamvu, m'malo moika maso awo pa mavutowo. M'malo mwake anayang'ana maso awo pa Mulungu ndi malonjezano ake pa anthu ake. Wolembe Ahebri akuyang'ana pa anthu ambiri amene chikhulupiliro chawo chinalimbikitsidwa osati pakukhazikika pa mavuto koma pakuyang'ana maso awo pa Yesu.

Zikuoneka zoyenera kuti mu chaka chino cha mantha komanso zinthu zokhudza zoti sizinachitikepo, kuti tilingalire za amuna ndi akazi achikhulupiliro chachikulu amenewa, kuphunzira kudzera ku chitsanzo chawo m'mene tingayang'anire maso athu pa Yesu, amene analonjeza chikondi komanso chisamaliro kwa ana ake onse, ngakhale mu namondwe wandiweyani. Chonde werengani ndime zolembedwa mu kabuku kano pamene ogwira ntchito ku Namikango akulingalira kwambiri pa za mutu umenewu oyang'ana maso athu pa Yesu.

-Eric Gephart

Yesu Ndiye Mphamvu Yathu

Tiri kukhala mu nthawi yovuta imene moyo wathu wa chikristu komanso wa thupi ukukumana ndi mayesero komanso mazunzo osiyanasiyana. Chifukwa cha umunthu wathu tikhonza kukhala ndi maganizo oti mayankho amavuto athu tingakwanitse kuwapeza tokha. Kunena zoonza ife mwatokha sitingathe kupambana nkondo kapena mavuto ali onse omwe angabwere m'moyo mwathu ngati siti yang'ana kwa Yesu Khristu. Tidzindikire kuti ife siwoyamba kukumana ndi masautso. Alipo anthu ambiri amene anakumana ndi masautso koma anayang'anabe pa Mulungu ndipo anapambana.

Nthawi zambiri tikakhala pa mtendere sikawiri kawiri kuganizira za Mulungu koma mavuto akatipeza mpamene ambiri aife timaganiza zoyang'ana kwa Mulungu. Komatu tikuyenera kudzindikira kuti Mulungu samatisiya amakhala nafe nthawi zonse ndipo Mulungu sasintha. Tikuyenera kukhala ndi chikhulupiliro pa Yesu Khristu chifukwa Iye samasintha chikondi chake pa ife. Muchipangano chakale timawerenga za Abrahamu. Iye anakhala zaka zambiri opanda mwana. Ngakhale zinali chomwechi Abrahamu anakhala omverabe Mulungu m'moyo wake wonse ndipo ali m'masiku aukalamba. Mulungu anadalitsa banja lake ndi mpatso ya mwana, Isake, monga mwalonjezo. Nzachidziwikire kuti banja la Abrahamu linadzala ndi Chimwemwe pakubadwa kwa mwanayo. Mulungu sanama; chomwe wachinena amachikwaniritsa. Komabe mwanayu atakulirapo, Abrahamu anaudzidwa ndi Mulungu kupanga chinthu chomwe chinali chovuta kuchilandira. Mulungu anamuuzira kuti “tengatu mwana wako, wamwamuna wayenkayo, Isake, amene ukondana naye, numuke ku dziko la Moriya; numpereke iye kumeneko nsembe yopsereza pa limodzi la

Genesis 22:2

Tengatu mwana wako, wamwamuna wayenkayo, Isake, amene ukondana naye, numuke ku dziko la Moriya; numpereke iye kumeneko nsembe yopsereza pa limodzi la mapiri lomwe ndidzakuuza iwe.

mapiri lomwe ndidzakuuza iwe” (Genesis 22:2).

Inali nthawi yovuta kwa Abrahamu poganizira kuti anthu amitundu amaperekanso nsembe ana awo, zomwe Mulungu anadana nazo. Koma iye pokhala kuti nthawi zonse amayang'ana kwa Mulungu anadziwa mauwo kuti anali Mulungu. Abrahamu sanaganize zothawa kapena kutsutsana naye Mulungu chifukwa anali pa ubale wabwino ndi Iye. Izi zinakhala chomwechi chifukwa Abrahamu analibenso kwina koyang'ana koma kwa Mulungu, kotero kunali kosavuta kumumvera.

Lero lino a khristu tikudusa mu nthawi zowawitsa kotero kuti zikufunika kuti tiyang'ane kwa Yesu Khristu chifukwa ndi komwe kuli mayankho a mavuto athu onse. Anthu ambiri akakumana ndi zotsamwitsa m'moyo wawo amasankha kupita kwa sing'anga kuti akathandidzidwe ndipo m'malo moti athandizike amakhumudwitsidwa.

Tikadalira munthu tidzakhumudwa chifukwa munthu adzalephera komanso samasunga pangano nthawi zonse. Onani Abrahamu pamene amadutsa mu nyengo yovuta kuti apange chiganizo choti atsature, iye anasankha kumvera Mulungu. Mwa umunthu, Iye anadikilira mwana kwa nthawi yaitali atamupeza, monga kholo lina liri lonse akanakonda kuti akhale naye. Mulungu anamulamula kuti apereke mwanayo nsembe, sizinali zophweka, koma iye anadziwa kuti anampatsa mwanayo anali Mulungu yemweyo ndipo anali ndi chikhulupiliro kuti Mulunguyo

ali ndi mphamvu zonse pa mwanayo.

Mulungu amagwira ntchito mosiyana ndi momwe ife timagwilira. Nthawi zina timaona ngati nthawi ikuchedwa kapena anthu akutisokoneza osadziwa kuti Mulungu akufuna atipambanitse. Abrahamu anafunsidwa kupereka nsembe mwana wake amene anali oti azakwaniritse lonjezo lomwe iye anapanga ndi Mulungu. Iye anaonetsa kukhazikika m'chikhulupiliro chake pa Mulungu pamene anaudza ananyamata kuti “khalani kuno ndi buru, ine ndi mwanayu tipita uko, ndipo tikapemphera ndi kubweranso kwa inu” (Genesis 22:5). Awa ndi mau achikhulupiliro kuchokera kwa Abraham, ngakhale Mulungu anamulamula kupereka mwana wake nsembe. Iye potsanzikana ndi anyamata ake sanayankhule mokaika kapena kudandaula, anadziwa kuti mwanayo akabwera naye. Nthawi zina tikafika munyengo zowawitsa timataya mtima kumadera nkhawa chifukwa timaziyang'ana tokha osati Mulungu. Umphawi ukakula timadandaula mkumaganiza kuti zinthu sizimayenera kutero. Tiyeni tidzidalira Mulungu munyengo zonse zomwe tikudutsamo, pamavuto komanso pa mtendere. Abrahamu moyo wake onse amadalira Mulungu ndipo amadziwa kuti alibe mphamvu iliyonse pamwanayo ndi chifukwa analolera kuyenda ulendo wa masiku atatu pofuna kumvera Mulungu.

Mulungu anampatsa Abraham mwana wa nkhoa kuti apereke nsembe m'malo mwa Isake chifukwa anaona pansa pa mtima wa Abrahamu kuti samangopanga mwa chipha maso koma anali pa ubale wabwino ndi Iye. Tikamapereka zopereka zathu, kapena pofuna kutumikira Mulungu, tikuyenera kutumikira ndi mtima wathu wonse. Zimenezi zimaonetsa kuti tikumudalira Iye m'magawo onse amoyo wathu.

Zomwe Mulungu anachita pompempha Abrahamu kupereka mwana wake chinali chithunzi thunzi cha zomwe Mulungu adzachite pofuna kuombola anthu ake ku

ukapolo wa uchimo. Iye anakonzeratu kuti adzayanjanitse anthu ake kwa Iye mwini ndikutipanga kukhala ana ake osatinso akapolo a tchimo. Paulo mukalata yake yolembera Agalatiya anati, “koma pokwaniridwa nthawi, Mulungu anatuma mwana wache, wobadwa ndi mkazi, wobadwa wakumvera lamulo, kuti ife tikalandire umwana. Ndipo popeza muli ana, Mulungu anatumiza Mzimu wa mwana wache alowe m'mitima yathu wofuula Abba, Atate. Kotero kuti sulinso kapolo, koma mwana, ngati mwana, wolowa nyumbanso mwa Mulungu” (Agalatiya 4:4 -7). Lero lino ife ndife opulumutsidwa si mwa mphamvu yathu koma Mulungu ndiye anakonza kuti ife tikalandire chipulumutso kudzera mu imfa ya mwana wake. Moyo wathu ukuyenera kulumuliridwa ndi Mzimu Woyera chifukwa Mzimuyo salinso kutali koma ali mwa ife. Chifukwa choti Mzimu woyera ali mwa ife komanso ndife ana ake a Mulungu kudzera mu imfa ya Yesu Khristu, tiyenera kuyang'ana pa Yesu ameneyu pamene takomana ndi mavuto kapena mayesero ena ali onse.

Dziko lonse la pansa likulira chifukwa cha mliri wa COVID 19 omwe wavuta kwambiri. Isanabwere nthendayi anthu anali otanganidwa kukaonera mpira, kupita kumalo azisangalalo, ndi kupanga zonse zokondweretsa moyo. Koma lero dziko lonse liri chete, munthu aliyense akufuna kupulumutsa moyo wake. Nthawi imeneyi inafunika kuti tonse timamatire pa Yesu. Anthu akumwalira, ndipo azachipatala akuyetsetsa kugwira ntchito molimbika kuti apulumutse anthu ku mliri umenewu. Zikufunika kuti ife akhristu tiyang'ane kwa Yesu kupempha kuti atichotsere vuto limeneli kuonjezera pa kutsatira malangizo akuchipatala. Mulungu wathu ndi wa mphamvu ndipo ife tikungofunika timamatire pa Iye munthawi imeneyi ndipo miyoyo yathu ilimbikitsika ngakhale tikudutsa munthawi yovuta ngati imeneyi.

Ngati sitiayang'ana kwa Yesu titaya

chikhulupiliro chifukwa vutoli ndi lalikulu. Ophunzira a Yesu tsiku lina ali mungalawa pakati pa nyanja chikhulupiliro chawo chinayesedwa ndipo Yesu anaonekera kwa iwo koma iwo sanathe kumzindikira. Petro ndi a nzake amatsutsana ataona munthu ofanana ndi Yesu,

“Koma pomwepo Yesu analankhula nawo nati limbani mtima, ndine, musaope. Ndipo Petro anamyankha Iye nati, Ambuye, ngati ndinutu, mundiuze ndidze kwa Inu pamadzi. Ndipo Iye anati, idza. Ndipo Petro anatsika m’ngalawa, nayenda pamadzi, kufikira kwa Yesu. Koma m’mene iye anaiona mphepo anaopa, ndipo poyamba kumira, anafuula, nati, Ambuye, ndipulumutseni ine!” (Mateyu 14:27 – 30).

Moyo wathu sungayende opanda Yesu. Tikhonza kuyesera koma sitingapambane. Vuto lomwe ophunzira amadutsamo limaoneka lalikulu pamanso pao chifukwa sanayang’ane kwa Yesu. M’mene Petro anayamba kuyenda akuyang’ana kwa Yesu, iye mphamvu zinabwera nayamba kuyenda pa madzi. Atangochotsa maso ake pa Iye nthawi yomweyo anayamba kumila. Pomwe zinthu zafika pa dziko lonse ngati anthu sitiayang’ana kwa Yesu mavuto athu apitilira kuipira ipirabe. Tikufunika maso athu tiyang’ane pa Yesu ndi chikhulupiliro chonse kuti atithandize mu nthawi yovutayi chifukwa Yesu salephera. Koma tikayang’ana pa mavuto omwe tikukumana nawo, tikhala ndi mantha ndipo chikhulupiliro chathu chigwedezeka.

Paulo polimbikitsa Mpingo kudera la Filipi anati, “ndikhonza zonse mwa Iye wondipatsa mphamvuyo”(Afilipi 4:13). Kusonyeza kuti munthu wina aliyense yemwe ndi mkhristu mphamvu yake pamane akudutsa m’masautso imachokera kwa Khristu Yesu osati kwina ayi. Anthu ena akafooka, kuti akhale ndi mphamvu amakhulupilira kuti amwe mankhwala ozunguza bongo kapena asute chamba ndiye akhala ndi mphamvu.

Koma zimenezi sizingathandize zimangopitiliza kuononga moyo wao. Paulo watisonyeza kuthekera kwa Mulungu mwa Yesu Khristu. Iye amalankhula mau awa ali mu ndende, ndipo awa anali mau ochokera mu mtima wa munthu okhazikika pa Yesu. Ngakhale anali pa mavuto koma mavuto sanakwanitse kumuchotsa pa Yesu, koma amamuyandikitsa chifupi ndi Mulungu. Tikuyenera tikhale ngati Paulo pakulimbika mtima ngakhale umunthu wathu ukukumana ndi manzunzo. Zimenezi siziri chomwecho ndi akhristu ambiri. Mavuto akabwera timalolera kusiya kudalira Yesu ndikukhulupilira zinthu zina. Tizindikire kuti pakutero timakhala tikudelera mphamvu ya Mulungu. Akhristu mavuto omwe dziko la pansu likudutsamo atipangitse kuyandikira chifupi ndi Mulungu, kuti iwo amene sakhulupilira Iye akathe kuzindikira za chikondi chomwe Mulungu ali nacho pa munthu wina aliyense. “Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero, kuti anapatsa mwana wache wobadwa yekha kuti yense wakukhulupilira Iye asatayike, koma akhale nao moyo wosatha” (Yohane 3:16). Mulungu chikondi chake anapereka kale pakupereka mwana wache kwasala ndikuti anthu onse akhulupilire Iye. “Chisomo cha Ambuye wathu Yesu Khristu chikhale nanu” (1 Atesalonika 5:28).

-Stanley Mkwanda

Kusintha kwa Miyoyo Kudzera Mu CHE

“Tsopano tikutha kulima chimanga popanda kuthira feteleza.”

Namikango Mission ikupitiriza pologalamu ya CHE ya uzimu ndi yokhudza miyoyo, imene yakhala yotsekula m’maso ku madera ambiri ku Malawi. Pologalamu ya

“Kulima Njira ya Mulungu” yakhala ikupitirira kubweretsa kusintha kwakukulu kwa anthu amene anayilandra bwino m’madera onse amiyoyo yawo. Kumbali ya zachuma, alimi achepetsa kuchuluka kwa feteleza wa kusitolo amene amagula mu zaka za m’mbuyomu pafupifupi ndi theka. Ena anasiiratuso kugwiritsa ntchito feteleza wa mankhwala; akugwiritsa ntchito manyowa okha pakulima chimanga ndipo akukololabe zokolola zochuluka. Izi zachepetsa kudalira ngongole kumene ngongole zambiri zimene zimatengedwa zimapita ku ulimi makamaka ku feteleza.

Izi zinabweretsanso chithonhozo kwa alimi amene adamvetsa ndi kulandira “Kulima Njira ya Mulungu.” Rodrick Sinoya ndi Rosert Mtambo ndi alimi achitsanzo ochokera ku Mangochi omwe anaphunzira ulimiwu pansi pa pologalamu ya CHE ya “Kulima Njira ya Mulungu”. Akuchitira umboni kuti ndizotheka Kulima chimanga popanda kuthira feteleza wa mankhwala komanso mkumakolola zokolola zochuluka. Malingana ndi Rodrick, “Ndinalima Njira ya Mulungu pa malo okula mamita 50x60. Ndinalima chimanga mu nyengo ya 2019-2020 ya ulimi ndipo ndinathira manyowa a kompositi okha ndi kutsatira njira yozulira udzu imene mlangizi wathu wa ku Namikango anatiphunzitsa. Sindinaganizirepo zakuti ndingaone chimanga chamtundu umenewu, koma ndili ndi chimanga ngakhalenso kuposa amene anathira feteleza mpaka akuba anayamba kundibera chifukwa cha nsanje. Chimanga chinakula bwino kwambiri! Ndikuyamika Mulungu ndi Namikango chifukwa cha kulowerera ku moyo wa uzimu komanso wa ku thupi. Ndikulangiza alimi anzanga kuti atsate njira imeneyi ya “Kulima Njira ya Mulungu” ndi kuikira umboni pamapeto pake.”

Rodrick wakhalanso m’dalitso ku Mpingo wa Khristu; iye anabatizidwa mu October pamene anabwera pa maphunziro achiwiri atamva kulalikidwa kokhudza moyo

wochuluka mwa Yesu kuchokera kwa alimi anzake achitsanzo komanso mphunzitsi wa CHE. Izi zikuonetsa kuti CHE ikukolola zokolola za uzimu komanso za kuthupi m’miyoyo ya anthu ku Malawi. Rosert anatsimikiziranso zomwe Rodrick ananena pamene tinawayendera onse ku Mangochi pa ulendo woyang’anira ndi kutsatira alimi achitsanzo a mupologalamu ya Kulima munjira ya Mulungu. Iye ananena umboni waukulu wa zomwe zinachitika ku madera awo; iye anati “anthu ambiri akufuna kutsatira Kulima Njira ya Mulungu ataona kuthekera kokolola zochuluka popanda kulowetsa ndalama zambiri. Tsopano ndimalima chimanga kawiri pa chaka, chilimwe ndi dzinja. Mu zaka ziwiri zapitazo Ine ndi banja langa sitinapite kokagona ndi m’imba mopanda kanthu. Tikuyamikira maphunzirowa omwe tikupindula nawo mu ulimi ndi m’mau a Mulungu.”

Ku Namikango, timakhulupilira kuti kudzera mu pologalamu ya CHE ya za ulimi ndi umoyo, pamodzi ndi mau a Mulungu, yabweretsa ndipo ikubweretsabe kusintha kwakukulu m’miyoyo imene tikuitumikira madera onse. Pamwamba pa Kulima Njira ya Mulungu, alimi achitsanzo okwana 65 anaphunzitsidwanso m’mene angapangire dongosolo la chuma la pa chaka, kusunga marekodi ndi dongosolo la ulimi wa mitengo. Izi zathandiza kwambiri m’makomo mwawo pamene ambiri aiwo ayamba kupanga malonda ang’onoang’ono monga Juwisi wa Lemon-grass, Juwisi wa malambe, Juwisi wa chidede, kungotchula zochepe. Uku ndi kukula bwino kwa moyo wa zachuma pamwamba pa kuchepetsa feteleza ogwiritsa ntchito. Ndi pempho lathu ku mpingo ndi kudera kuti ayambe kugwiritsa ntchito mapologalamu auzimu ndi kakhaliidwe ka moyo kamene Namikango imapereka, ndi cholinga chokweza miyoyo yawo ndi kukwaniritsa moyo wochuluka umene unanenedwa ndi Yesu mu Yohane 10:10. Mukhoza kukhala mtsogoleri

wa kusintha pakumemeza magome/ mipingo yanu kapena dera lanu ku maphunziro amenewa omwe akuthandiza kupanga moyo wabwino wa a Khristu komanso dera lanu.
-Faith L. Somanje

Ubwino wa Banki Mkhonde

Liu la Namikango lomwe lidalembedwa miyezi yapita m'mbuyomu, tidafotokodzera za VSL kapena kuti banki ya m'mudzi. Mwachidule, tidati, VSL ndi mau achidule am'chingelezi amene ndi Village Savings and Loans. Awa ndi magulu osunga ndi kubwereketsana ndalama. Tidaonetseranso ubwino ochuluka umene ma banki a m'mudzi amene ali pansu pa Namikango Mission alinawo. Mu Liu ili, tifotokozera zolinga zikuluzikulu zomwe zidapangitsa kuti Namikango Mission ikhazikitse ntchito yophunzitsa akhristu m'mipingo kusunga ndi kubwereketsana ndalama m'magulu komanso tifotokozera za momwe dongosolo la VSL limayendera.

Ntchito yophunzitsa akhristu kusunga ndi kubwereketsana ndalama inakhazikitsidwa ndi zolinga zikuluzikulu izi; Choyamba, kulimbikitsa akhristu m'mipingo kuti azidziwa kuti ali ndi udindo osamalira zomwe Mulungu adapeleka kwa ife anthu (zinthu monga chuma, nthawi, mphamvu, komanso luso la kachitidwe kamalonda). Cholinga chachiwiri ndikulimbikitsa chikhaliidwe chosunga ndalama, kagwilitsidwe ntchito kabwino ka chuma komanso kuti anthu adzidziimira paokha pankhani zachuma.

VSL ndi dongosolo limene limayamba ndi kuyendetsedwa palokha opanda chithandizo cha chuma chochokera kwina (Izi zikutanthauza kuti Namikango Mission, siipeleka thandizo la ndalama ngati anthu ayamba gulu losunga ndi kubwereketsana ndalama). Gulu likayamba

limadziyendetsa lokha potengera mfundo (malamulo) zomwe gululo lakhazikitsa. Zinthu zinai zomwe anthu okhala pagulu amachita akayamba gulu ndi kusunga ndalama, kubwereketsana, ndikubwenza ndi chiongola dzanja chochepa chimene gulu limagwilizana. Pakapita nthawi gulu limagawana ndalamazo.

Mu VSL anthu a pakati pa 15 mpaka 25 amapanga gulu limene mlangizi wa VSL amaliphunzitsa zokhudzana ndi ntchitoyi. Gulu limeneli limalemba malamulo komanso kusankha atsogoleri amene amatsogolera gululo. Ma membala onse ndiye amakhala eni ake agulu ndipo atsogoleri ndi anthu ongosankhidwa kutumikira gulu popatsidwa udindo ndi ntchito zoti azigwira. Gululi limakumana kamodzi pasabata pamene mamembala amasunga ndalama kudzera mu njira ya masheya. Mamembala amabwerekana ndalama zimene amayenera kubwenza pasanadutse masabata anayi. Ntchitoyi imachitika kwa miyezi 9 mpaka 12. Pomaliza, mamembala amagawana ndalama zomwe apeza potengera kuchuluka kwa kwa masheya amene aliyense alinawo. Panthawi imene mamembala akusunga ndikubwerekana ndalama zija, mlangizi amaliyendera gulu lija ndi kumaliwongolera zonse m'mene zikuyenera kukhalira. Gulu likagawana, mlangizi amayenera kuliona gulu lija ngati lakhwima kuti likhoza kuima palokha, kapena mwina likadali ndi zofooka zina. Ngati likadali ndi zofooka, mlangizi amapitiliza kuliyenderabe mu gawo lachiwiri. Mwa ntchito zina, gulu limakhalanso ndi thumba lapadera limene mamembala amathandizikira pa nthawi ya zadzidzidzi monga matenda ndi maliro.

Thumba lapaderali limagwira ntchito mu njira ziwiri zikuluzikulu. Njira yoyamba, thumbali limagwira ntchito ngati chithandizo kapena kuti mphatso. Chitsanzo, ngati membala wagulu kaya mwana wake wadwala, anzake agulu akhoza kugwilizana ndikutenga ndalama kuthumbali mkukamuona. Thumbali

limagwiranso ntchito ngati ngongole. Ngati membala wadwala kapena kukumana ndi vuto ladzidzidzi amatha kubwereka kuthumba limeneli ndipo amabweza mopanda chiongoladzanja chilichonse. Ndalama yosonkhedwa kuthumbali imayenera kukhala yofanana chifukwa imayenera kuthandiza mofanana.

Kodi ndondomeko ya ndalama za thumba lapadera imayenda bwanji? Ndalama izi siziyenera kuphatikizidwa ndi ndalama za masheya zomwe anthu amatha kubwereka mkumachitira malonda. Gulu limayenera kuika malamulo okhudza m'mene ndalama zadzidzidzi zizigwilira ntchito poganizira oyenera kulandira ndalamazi (momwe zingapezekere, momwe zingatulukire, momwe zingabwezedwere). Mamembala amayenera kugwilizana kuchuluka kwa ndalama zimene aliyense azisonkha pa mkumano ulionse zopita kuthumbali. Mamembala agulu amayenera kugwirizana za kuchuluka kwa ndalama za chithandizo chimene azipeleka pa mavuto kwa munthu amene wabvomelezeka kulandira thandizo kuchokera kuthumbali ndicholinga choti pasakhale kukondera. Iwo amayeneranso kugwilizana za kabwenedwe ka ndalamayi ngati padzakhale kufunika kutero. Ndipo ayenera agwilizanso za m'mene adzayendetsere ndalama zotsala ikadzakwana nthawi yogawana.

Ena mkumafunsa kuti chokhalira pagulu m'chiyani pamene ndekha nditha kusunga ndalama komanso kumachita malonda pandekha? Pa Chichewa pali miyambi yambiri imene imaonetsera kufunika kogwira ntchito ngati gulu. Mwambi odziwika kwambiri ndi uja amati, mutu umodzi susenza denga komanso wina ati kukhala awiri simantha. Anzathu achimwenye adaona kufunika kochita malonda limodzi. Mwachitsanzo, iwo amatha kusonkherana ndalama mkumachita bizinezi yaikulu zomwe zimawathandiza kupezanso phindu lochuluka pomwe kuno ku Malawi timakhumbabe kuchita malonda aliyense

payekha. Akhristu ambiri akhala akudandaula kuti sangayambe bizinezi chifukwa iwo alibe mpamba okwanira. Koma atapezeka anthu angapo mkusonkherana, anthutu atha kuchita zodabwitsa zomwe zikhoza kusintha miyoyo yawo komanso ya iwo amene awazungulira.

Kuchita zinthu pagulu kumathandiza kugawana nzeru zosiyasiyana za m'mene tingakwanilitsire zinthu zina monga malonda, momwe tingayendetsere mabanja, mpingo, dera ngakhaleenso dziko. Kukhala pa gulu kumathandizanso kuti anthu apeze mwayi wa ngongole zochitira mabizinezi ang'onoang'ono. Mukhonza kuchitira umboni kuti mabungwe obwereketsa ndalama, samavuta kupeleka ngongole kwa anthu amene alipo angapo kusiyana ndi munthu m'modzi.

Magulu amene akhazikitsidwa ndi Namikango anayamba kupindula mochuluka ndi dongosolo limeneli ngakhale anthu ena anali ndi malingaliro oipa okhudza VSL. Chiwerengero cha abale ndi alongo omwe akupanga banki ya m'mudzi pano chikukulabe ndipo ambiri kuno ku Malawi ngakhaleenso ku Mozambique ndi ku Zambia akufuna Namikango itawafikiranso. Mamembala akutha pano kudziimira paokha pachuma komanso lero amatha kutumikira Mulungu mosavuta chifukwa kudzera mu magulu amenewa, anthu amaphunzira kutsogolera nyimbo za Mulungu, amaphunzira kuwerenga Mau a Mulungu, kumasulira malemba ndi zina zambiri zothandizira kuti moyo wa uzimu ndi wa kuthupi upite patsogolo. Izi zikupangitsa moyo wa anthu akumudzi kukhala wa mphumphu. "Yesu anati, siikudza mbala, koma kuti ikabe, ndikupha ndikuononga, ndadza ine kuti akhale nawo moyo, ndi kukhala nawo wochuluka" (Yohane 10:10).

-Blazio Styford

Zolengeza

Southern Africa International Lectureship

- Msonkhano wa SAIL (Southern Africa International Lectureship) chaka cha 2020 umene umayenera kuchitikira ku Bulawayo unalepheretsedwa chifukwa cha matenda a Coronavirus.
- Mkumanowu udzachitika m'chaka cha 2021 ku Bulawayo ndipo zokonzekera zonse zidzadziwika kudzera ku komiti yoonza za mayendedwe.

Utumiki wa pawalesi

- Tikudziwitsa aliyense amene amatsatira pologalamu ya 'Kodi Muli Pati' pa walesi ya TWR(Trans-World) kuti pologalamuyi ikuwulutsidwabe Lamulungu lililonse kuyambira nthawi ya 6:30 mpaka 6:45. Koma, pamene walesiyi imagwirira inasinthidwa malingana ndi madera osiyanasiyana. Choncho, mukuuzidwa kuti mukuyenera kuyang'ananso mogwirira mwatsopanomu.
- Awa ndi ena mwa malo ogwirira owerengeka chabe: Blantyre 90.6, Thyolo 101.8, Mangochi 105.7, Dedza 98.5, Lilongwe 106.3, Mchinji 96.7, Mvera 93.9, Karonga 106.3 and Ntchisi 90.7.

Pologalamu ya Bible School

- Namikango idzayamba Discipleship Training Institute mu 2021 monga mwakulengeza kumayambiriro. Zina zokhudza pologalamu yonse zidzaperekedwa posachedwapa kwa ofuna kulembera.

Namikango Outreach Programmes (Utumiki wa Namikango Wotumikira Madera ena)

- Chifukwa cha Coronavirus, kuyendera mipingo konse komanso misonkhano ya chitukuko inaimitsidwa kuyambira mwezi wa April mpaka pamene zinthu zidzabwererense m'chimake.
- Tikulimbikitsa mipingo ndi magulu achitukuko kutsatira njira zonse zopewera zimene zaikidwa ndi unduna wa zaumoyo pofuna kupewa kufalikira kwa matenda a Coronavirus.

Odwala

- Tipitirize kupempherera anthu awa:
 - M'bale J.C. Katete ku Chingale, Zomba
 - M'bale B.S. Mbewe ku Liwonde, Machinga
 - M'bale Lendal Wilks ku America

Omwalira

- M'bale Kachingwe mlaliki wakale wochokera kwa Dzanjo, Phalombe anamwalira pa 8 March ndipo anaikidwa m'manda pa 9 March 2020.